NATIONAL REGISTRATION BUREAU

KUSINTHA KWA UDINDO OYANG'ANIRA NTCHITO YA KALEMBERA WA MA UKWATI KUPITA KU NATIONAL REGISTRATION BUREAU (NRB)

Bungwe la National Registration Bureau (NRB) likudziwitsa anthu onse mdziko muno kuti kutsatira kusintha kwa lamulo loona za ma ukwati ndi mabanja la Marriage, Divorce and Family Relations Act, (MDFRA) CAP 25:01, udindo oyang'anira ntchito ya kalembera wa ma ukwati wachoka ku ofesi ya Registrar General kupita ku bungwe la NRB. Kamba kakusinthaku, tsopano nkulu wa bungwe la NRB ndi amene aziyang'anira ntchito za ma ukwati m'dziko muno.

Kamba ka kusinthaku, tsopano bungwe la NRB liziyang'anira ntchito za ma ukwati monga: kumanga ma ukwati, kupereka ziphaso za ma ukwati ya mitundu yonse, komanso kulemba ma ukwati.

Bungwe la NRB likudziwitsanso a Malawi kuti ma ukwati onse omwe amachitikira ku ofesi ya Bwanamkubwa (DC) apitilira kumangidwa ku ma ofesiwa, ndipo ma ukwati omwe amachitikira m'malo a chipembedzo apitilira kumangidwa m'malo achipembedzo ovomelezeka. Pakadali pano, bungwe la NRB likukumana ndi onse okhudzidwa pa nkhani za ma ukwati ndipo posachedwapa lidziwitsa anthu onse ndondomeko zina zotsatira zokhudza momwe ntchito za ma ukwati ziziyendera m'dziko muno.

Ngati mukufuna kudziwa zambiri, imbani lamya ku NRB pa: **488**; **0111700700**; kapena SMS/WhatsApp: **0987074071** ndi **0987074073** kapenanso lembani email ku: callcentre@nrb.gov.mw.

Patrick Machika

PRINCIPAL SECRETARY

NATIONAL REGISTRATION BUREAU